ULIMI WA THONJE



MAWU OYAMBA

Thonje ndi imodzi mwa mbewu zimene alimi amalima kuti apeze ndalama muno m'Malawi.
Ngakhale zili choncho, ulimi wa thonje wakhala ukukumana ndi mavuto ambiri amene achititsa kuti alimi azikolora thonje lochepa. Ena mwa mavutowa ndi kuchuluka kwa tizirombo ndi matenda, komanso kusatsatira njira zovomerezeka pa ulimi wa thonje. Alimi akulimbikitsidwa kuti atsatire njira zivimerezeka za ulimi kuti ulimi wa thonje upite patsogolo.

MITUNDU YA THONJE YOVOMEREZEKA

Gulani mbewu kwa ma agulo dila ovomerezeka ndi boma ndipo onetsetsani kuti;

- Mbewu yalongedzedwa mpepala kapena mu saka labwino komanso lolembedwa bwino
- Onetsetsani kuti mbewu yalembedwa dzina, mtundu, makilogalamu, dzina komanso adilesi ya ogulitsa. Musagule mbewu yoyezetsa pa msika

MITUNDU YA MBEWU YA THONJE YA MAKOLO

- **Makoka 2000:** Imachita bwino m'madera a chigwa cha mtsinje wa Shire. Mutha kokulola thonje lokwana makilogalamu opitilira 3000 pa hekitala imodzi ikasamalidwa bwino ndipo imacha pakatha masiku 97 kuchokera tsiku linene mwabzala.

- **RASAM 17:** Imachita bwino m'madera a mphepete mwa nyanja. Mutha kokulola thonje lokwana makilogalamu opitilira 3000 pa hekitala imodzi ikasamalidwa bwino ndipo imacha pakatha masiku 121 kuchokera tsiku linene mwabzala.

- **IRM 81:** Imachita bwino m'madera okwera. Mutha kokulola thonje lokwana makilogalamu opitilira 500 pa hekitala imodzi ikasamalidwa bwino ndipo imacha pakatha masiku 122 kuchokera tsiku linene mwabzala.

- **QM301:** Imachita bwino m'madera a mphete mwa Nyanja. Mutha kokulola thonje lokwana makilogalamu opitilira 3500 pa hekitala imodzi ikasamalidwa bwino ndipo imacha pakatha masiku kuyambira 150 mpaka 160 kuchokera tsiku limene mwabzala. Mbewuyi ndi yopilira ku majasidi ndi kangaude ofiira
- **QM 201:** Imachita bwino m'madera a chigwa cha mtsinje wa Shire Mutha kokulola thonje lokwana makilogalamu opitilira 3500 pa hekitala imodzi ikasamalidwa bwino ndipo imacha pakatha masiku kuyambira 150 mpaka 160 kuchokera tsiku limene mwabzala. Mbewuyi ndi yopilira ku tizilombo toyamwa madzi a m'bewu.
- **QM 302:** Imachita bwino m'madera a mphepete mwa Nyanja. Mutha kokulola thonje lokwana makilogalamu opitilira 3000 pa hekitala imodzi ikasamalidwa bwino ndipo imacha pakatha masiku kuyambira 160 mpaka 170 kuchokera tsiku limene mwabzala. Mbewuyi ndi yopilira ku toyamwa madzi a m'mbewu.
- **QM 303:** Imachita bwino m'madera onse. Mutha kokulola thonje lokwana makilogalamu opitilira 3000 pa hekitala imodzi ikasamalidwa bwino ndipo imacha pakatha masiku kuyambira 160 mpaka 170 kuchokera tsiku limene mwabzala. Mbewuyi ndi yopilira ku toyamwa madzi a m'mbewu

Bzalani mbewu ya thonje yovomerezeka kuti mukolore zochuluka. Alimi akulimbikitsidwa kubzala njere za thonje zovomerezeka komanso zomwe zilibe ti thonje totsalira. Mbewu ya thonje yovomerezeka imapezeka ku ofesi yowona za kafukufuku yak u Makoka.

MITUNDU YA MBEWU YA THONJE YA MAKONO

- **MAHYCO C 567:** Imachita bwino m'madera a mphepete mwa Nyanja. Mukhoza kukolora thonje lokwana ma kilogalamu 4000 pa hekitala imodzi ndipo imacha pakatha masiku kuyambira 160 mpaka 170 kuchokera tsiku limene mwabzala.

- **MAHYCO C 569:** Imachita bwino m'madera onse kumene kumalimidwa thonje. Mutha kukolora makilogalamu okwana 4000 pa hekitala imodzi ndipo imacha pakatha masiku kuyambira 170 mpaka 180 kuchokera tsiku limene mwabzala.
- **MAHYCO C570:** Imachita bwino m'madera a chigwa cha mtsinje wa shire komanso m'madera okwera pan'gono. Mutha kukolora thonje lokwana makilogalamu 4000 pa hekitala imodzi ndipo imacha pakatha masiku kuyambira 170 mpaka 180 kuchokera tsiku limene mwabzala.
- **MAHYCO C 571:** Imachita bwino m'madera onse. Mutha kukolora Recommended for cultivation in all areas. Mutha kukolora thonje lokwana makilogalamu 4000 pa hekitala imodzi ndipo imacha pakatha masiku kuyambira 170 mpaka 180 kuchokera tsiku limene mwabzala.
- **MAHYCO C 577:** Imachita bwino m'madera a mchigwa cha mtsinje wa Shire. Mutha kukolora Recommended for cultivation in all areas. Mutha kukolora thonje lokwana makilogalamu 4000 pa hekitala imodzi ndipo imacha pakatha masiku kuyambira 160 mpaka 170 kuchokera tsiku limene mwabzala.
- **MAHYCO C579:** Imachita bwino m'madera onse. Mutha kukolora Recommended for cultivation in all areas. Mutha kukolora thonje lokwana makilogalamu 4000 pa hekitala imodzi ndipo imacha pakatha masiku kuyambira 170 mpaka 180 kuchokera tsiku limene mwabzala.
- **MAHYCO C608:** Imachita bwino m'madera onse. Mutha kukolora Recommended for cultivation in all areas. Mutha kukolora thonje lokwana makilogalamu 4000 pa hekitala imodzi ndipo imacha pakatha masiku kuyambira 160 mpaka 170 kuchokera tsiku limene mwabzala.

- **Mtundu wa thonje wa Bt**

Mbewuyi ndi yopilira ku mbozi

- **MAHYCO C 567 BG II:** Imachita bwino m'madera onse amene kumalimidwa thonje. Mukhoza kukolora thonje lokwanira ma kilogalamu 4000 pa hekitala imodzi muisamalira bwino ndipo iacha pakatha masiku kuyambira 170 mpaka 180 kuchokera tsiku limene munabzala.
- **MAHYCO C 569 BG II:** Imachita bwino m'madera onse amene kumalimidwa thonje. Mukhoza kukolora thonje lokwanira ma kilogalamu 4000 pa hekitala imodzi muisamalira bwino ndipo iacha pakatha masiku kuyambira 170 mpaka 180 kuchokera tsiku limene munabzala. Mbewuyi ndiyopilira ku tizilombo toyamwa madzi a m'mbewu
- **MAHYCO C 570 BGII:** Imachita bwino m'madera onse amene kumalimidwa thonje. Mukhoza kukolora thonje lokwanira ma kilogalamu 4000 pa hekitala imodzi muisamalira bwino ndipo iacha pakatha masiku kuyambira 170 mpaka 180 kuchokera tsiku limene munabzala.
- **MAHYCO C 571 BG II:** Limachita bwino m'madera onse amene kumalimidwa thonje. Mukhoza kukolora thonje lokwanira ma kilogalamu 4000 pa hekitala imodzi muisamlira bwino ndipo imacha pakatha masiku kuyambira 170 mpaka 180 kuchokera tsiku limene munabzala. Imapilira ku tizilombo toyamwa madzi a m'mbewu

KALIMIDWE KA MBEWU YA THONJE

Kukonza malo: Konzani malo moyambilira mukangomaliza kukolola. Tipulani mozama ndi masentimita 15 mpaka 25 kuti mizu izilowa pansi mosavuta. Konzani mizere mosemphanitsa kuti madzi azisuka mnthaka.

Kubzala: Bzalani thonje moyambilira ndi mvula yobzalira yoyamba ikagwa mokwanira.

Bzalani mbewu ya thonje la lokolo pa mizere yotalikirana masentimita 75 mpaka 90 pa ma phando otalikana masentimita 30 mpaka 60. Bzalani njere zopanda tithonje totsalira 5 mpaka 7 pa phando, ndipo patulirani kuti pa phando lililonse pakhale mbewu zitatu pa mpata wa masentimita 60, komanso mbewu imodzi pa phando pampata wa masentimita 30. Bzalani mbewu ya thonje mozama masentimita awiri panthaka ya chinyezi ndipo bzalani mbewu mozama masentimita 2.5 mpaka 3.2cm ngati mukubzala pa nthaka youma.

Bzalani thonje la makono komanso la Bt pa minzere yotalikana mita imodzi pa ma phando otalikana masentimita 45. Ngati mvula yagwa bwino, bzalani njere imodzi pa phando ndipo ngati mvula siinangwe bwino, bzalani njere ziwiri pa phando. Bzalani njere za thonje mozama masentimita awiri mpaka atatu mu nthaka ya chinyezi.

Kupalira: Palirani m'munda wa thonje ndi khasu kapena poperani mankhwala ophera udzu. Onetsetsani kuti m'munda wa thonje mulibe tchire nthawi iliyonse popalira udzu ukangomera.

Kuthira feteleza: Thirani fetereza okulitsa wa 23:10:5+6S+1Zn pa mulingo wa makilogalamu 100 pa hekitala imodzi pakatha masabata atatu mbewu ya thonje ikaphuka. Thirani fetereza okwana capu imodzi ya nambala 5 kapena okwanira mu chitsekelero cha botolo la kokakola lochotsa cha mkati pa phando lililonse.

Sungunulani ma galamu 40 a feteleza wothira kudzera mmasamba a mbewu m'madzi okwana ma lita 15 ndikipopera m'munda wa thonje pakatha masabata 7 mbewu ikaphuka. Poperani mankhwalawa pa malo okwana 0.1 ha kamodzi pa masabata awiri alionse.

Thirani fetereza obeleketsa wa CAN pa mulingo wa makilogalamu 40 kapena wa Urea pa mulingo wa mailogalamu 24 pa hekitala imodzi pogwiritsa ntchito kapu nambala 5 kapena chitsekelero cha botolo la kokakola lochotsa cha mkati pa phando lililonse mphukira zikayamba kuoneka.

Kuthira manyowa: Mukhoza kuthira manyowa m'munda wa thonje pobzala mmalo mwa fetereza okulitsa. Thirani fetereza obeleketsa thonje likaya maluwa kuti libereke bwino.

KUTETEZA THONJE KU TIZILOMBO

Thonje limaononge ka kwambiri ndi tizilombo. Choncho alimi akulimbikitsidwa kubzala mbewu ya ukhondo komanso yothira mankhwala.

Alimi akulimbikitsidwa kuyendera munda wa thonje ndikuunika mbewu zochepa chabe kuti aone ngati wagwidwa ndi tizilombo kuti apange chiganizo chopopera mankhwala.

Alimi aykuyenera kuyendera minda ndikuunika mbewu pa malo owerengeka kuti aone ngati kuli kofunika kupopera mankhwala.

NJIRA ZOYENDERA MINDA

Onani chithunzi 1

Alimi akuyenera kupopera mankhwala ovomerezeka kuti aphe tizilombo todya masamba, semi loopers, mbozi, chammatowo, ziwala, nsabwe ndi kangaude ofiira.

Mbozi zimagwira kwambiri mbewu ya thonje ndipo zimaononga thonje lenilenilo. Tizilombo toyamwa madzi a m'mbewu timaononganso kwambiri thonje. Tizirombo todya masamba monga ziwala zimaononganso thonje. Alimi akuyenera kupopera mankhwala opheraa tizilomboti pokhapokha ngati chiwerengelo cha tizirombo tadutsa mlingo oikika.

MITUNDU YA THONJE YA BT SIIMAGWIDWA NDI MBOZI

Alimi akuyenera kuonetsetsa kuti mankhwala amene akugula ali ndi izi:

- Nambala yochokera ku bungwe loona za mankhwala la Pesticides Control Board
- Botolo kapena pepela likhale lotseka bwino

- paketi kapena botolo likhale ndi dzina la mankhwala
- Akhale ndi tsiku limene mankhwala azaonongekele.
- Akhale ndi tsiku limene anapangidwa
- Akhale ndi mulingo, kapena kalemeledwe

Kafunseni za kagwiritsidwe ntchito ka mankhwala koyenera kwa alangizi amene muli nawo pafupi, ndipo onetsetsani kuti mwataya botolo kapena paketi la mankhwala pa malo oyenerera.

KUKOLORA NDI KUSAMALA THONJE

Kukolora ndi kusankha

- Kolorani thonje ngati litatu kapena linayi latsegula pa mbewu iliyonse.
- Kolorano thonje pamene kunja kuli kouma.
- Gwiritsani ntchito masaka awiri aukhondo pokolora thonje. Ikani thonje loyera mthumba lina ndipo ikano thonje lokuda mthumba lina. Mukhozanso kusankha thonje mukakolola. Sankhani thonje pa mnthunzi ndipo ikani thonje loyera palokha ndi lokuda palokha.

KUSUNGA

- Sungani thonje mma belo a chiguduli kuti lisaonongeke
- Sungani ma belo a thonje pa malo okwera ndi ouma bwino.

KUZULA MICHAKALA YA THONJE

Alimi akuyenera kuzula ndi kuotcha michakala ya thonje akakolora kuti achepetse kufalikira kwa tizilombo

Dziwani izi: *Lamulo la ulimi wa thonje mdziko lino limanena kuti mlimi aliyense akuyenera kulembetsa mu kaundula wa alimi a thonje ku bungwe la Cotton Council of Malawi (CCM) chaka chilichonse*

Designed and Printed by
Agricultural Communication Branch
P.O. Box 594
Lilongwe

© 2019